Dipo la Yesu Ndi Mphatso ya Mulungu Yamtengo Wapatali Kuposa Zonse (Gawo 2)

Nkhaniyi yachokera m'mutu 5 wa buku lakuti, *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mozama zimene mumakhulupirira ndiponso zifukwa zake, fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, kenako ganizirani mmene mungafotokozere ena zimene mumakhulupirirazo.



KODI TIMAPINDULA BWANJI CHIFUKWA CHA IMFA YA YESU?

1 GANIZIRANI MOZAMA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi mukuganiza kuti anthu ena angayankhe bwanji?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

Nanga n'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Tingapeze madalitso ambiri chifukwa cha dipo la Yesu.

(Werengani mutu 5 m'buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 14 mpaka 17.)

Werengani Akolose 1:13, 14 ndi Aheberi 9:13, 14.

Kodi nsembe ya Yesu ingatithandize bwanji kuti tisamadziimbe mlandu kwambiri chifukwa cha machimo athu?

Werengani Aroma 6:23.

Kodi anthu okhulupirika adzapindula bwanji ndi nsembe ya Yesu mpaka muyaya?

Nsembe ya dipo la Yesu ingatithandize kuti tipeze madalitso ambiri pokhapokha ngati timaikhulupirira

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Tiziyamikira mphatso ya nsembe ya Yesu.

(Werengani mutu 5 m'buku lakuti *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 18 mpaka 22.)

Werengani Yohane 17:3 ndi 1 Yohane 5:3.

Kodi kuyamikira mphatso ya nsembe ya Yesu kungatithandize kuti tizichita chiyani?

Werengani Yohane 3:16 ndi Yakobo 2:26.

Kodi **kungonena** kuti timakhulupirira nsembe ya Yesu kumatanthauza kuti timaikhulupiriradi?

Kodi inuyo mungachite zinthu ziti posonyeza kuti mumayamikira nsembe ya Yesu

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI . . .

Ineyo sindikuona m'mene imfa ya munthu m'modzi yemwe anafa zaka zambirimbiri zapitazo ingandithandizire.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

Anthu ambiri anganenedi choncho. Koma ine ndimakhulupirira kuti imfa ya Yesu *imatithandiza* kwambiri pa moyo wathu chifukwa . . .

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji vesilo pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

WINA AKANENA KUTI . . .

Munthu kuti udzapulumuke umangofunika kukhulupirira Yesu basi.

MUNGAYANKHE KUTI . . .

N'zoona kuti tifunika kukhulupirira Yesu. Koma ndimakhulupiriranso kuti pali zambiri zimene tiyenera kuchita chifukwa . . .

_____

_____

Kodi mungawerenge lemba liti kuti mumuthandize?

_____

Kodi mungafotokoze bwanji vesilo pomuthandiza malinga ndi zimene amakhulupirirazo?

_____

www.jw.org © 2015 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania